EXAMINATION NO. ___________________________

# CHIRADZULU DISTRICT EXAMINATION BOARD

2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

## CHICHEWA

(100 malikisi)

**Lachiwiri, 19 March**

**Nthawi: 2h 15min**
**8:00am-10:15am**

**Dzina lanu**______________________________________________________________________
(yambani ndi lababmo)
**Dzina la Sukulu**_________________________________________________________________

**GAWO A (malikisi 30)**

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma osabzola 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu:
   ZOTSATIRA ZA CHILALA
   Mwa zina tsatani izi polemba.

   **Ndime yoyamba**
   - Fotokozani kodi chilala ndi chiyani
   - Zomwe zimayambitsa chilala ndi chani (mfundo ziwiri)
   - Zizindikiro ziwiri za chilala

   **Ndime yachiwiri**
   - Mavuto omwe amadza chifukwa cha chilala.
   - Fotokozani kodi chilala chimakhudza motani chuma cha dziko

   **Ndime yachitatu**
   - Anthu amatani kuti apeze chakudya nthawi ya chilala
   - Tchulani njira ziwiri zimene tingapewere chilala m'dziko.

**KAPENA**

2. Yerekezani kuti ndinu mlembi wa gulu la zaulimi m'dera lanu. Lembani kalata yopempha ngongole kwa mkulu wa zangongole. Bungwe la nzeru n'chuma P.O.Box 90 Chiradzulu.
   Mwa zina tsatani izi polemba:

   **Ndime yoyamba**
   - Cholinga cha kalata yanu
   - Gulu lanu liri m'dera liti?
   - Adayambitsa gulu limeneri ndi ndani

- Tchulani mitundu itatu ya mbewu zomwe mumalima.

**Ndime yachiwiri**

- Fotokozani mavuto omwe mumakumana nawo pagulu
- Ndi ndalama zingati zomwe mukufuna kubwereka
- Zikuthandizani motani ndalamazi akakubwerekani

**Ndime yachitatu**

- Kodi mukadzalephera kubweza ngongoleyi mudzachita chiyani?

**GAWO B** (malikisi 20)

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

Atadzidabwa Milika ,yemwe adali chisamba cha banja la a Msuma ,adauza anzake omwe amacheza nawo.Pakuti ena mwa anzakewo adali mauthu sadadziwe china chilichonse choti angamulangize mnzawoyo .Pagululi padali anamwali atatu omwe atamva zimene Milika amanena adangotsinzinirana. Adachita izi podziwa kuti bongololo sadzolera mafuta pagulu .Makamaka sadafune kulawulira amene anali asanagwe m’dothi .Pansi pamtima atsikanawa adadziwa kuti tsopano Milika ndi namwali mnzawo.Mmene zimachitika zonsezi n’kuti atsikanawo akuchokera ku madimba atadendekera madengu ndi msengwa za ndiwo zoti akadyere nkhomaliro.

Atsikana akuluakulu aja sadanene chilichonse pankhaniyo pakuti idali nkhani yofunika ntchembere .Omwe samadziwa kanthu amangomuseka Milika pakuti kwa iwo chilichonse chidali cha chachilendo. Mauthuwo adali Lekeleni, Nachanza ndi Elube.Enawa adali Tiwonge ndi Mtupa.Onse adali atsikana a M’mudzi mwa M’bebe.Mudziwu umatchuka ndi gule wa chintali.

Atafika kumudzi anamwali adadziwitsa amayi ake a Milika .Nthawi yomweyo amakewo adatengera nkhaniyo kwa nankungwi .Atamva izi nankungwiyo sadafune kuchedwa .Iye adakauza ntchemberegandule zapamudzipo.Ntchemberegandulezo zidatsinana makutu ndipo zidagwirizana zokhala naye pansi mtsikanayo .Kutacha adamuyitana Milika kuti akakumane naye m’kanyumba komata.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

a. (i) Kodi Milika adali wa m’banja liti?

______________________________________________________________(malikisi 1)

(ii) Ndindani omwe adamva zimene Milika ankanena ndipo ankangotsinzinirana?

______________________________________________________________(malikisi 1)

b. Chifukwa chiyani anamwali atatu aja adangotsinzinirana maso?

______________________________________________________________(malikisi 2)

c. (i) Kodi atsikanawa amachokera kuti?

______________________________________________________________(malikisi 1)

(ii) Tchulani mayina awiri a atsikana omwe ankamuseka Milika atanena zomwe zidamchitikira

______________________________________________________________

______________________________________________________________(malikisi 2)

d. Chifukwa chiyani mudzi wa M’bebe udali wotchuka?

______________________________________________________________(malikisi 2)

e. (i) Ndi ndani amene adakadziwitsa amayi ake a Milika zomwe zidamchitikira Milika?
_______________________________________________________________(malikisi 1)
(ii) Ndi ndani adakauza ntchemberegandule za pamudzi?
_______________________________________________________________(malikisi 1)

f. Pezani mawu m'nkhaniyi omwe matanthauzo ake ndi awa:
(i)mwana woyamba kubadwa
_______________________________________________________________(malikisi 1)
(ii) mtsikana osatha msinkhu
_______________________________________________________________(malikisi 1)

g. Perekani mawu otsutsana ndi mawu awa mu nkhaniyi:
(i) Akupita
_______________________________________________________________(malikisi 1)
(ii) Mauthu
_______________________________________________________________(malikisi 1)

h. Chifukwa chiyani Milika adakumana naye m'kanyumba komata?
_______________________________________________________________________
_______________________________________________________________(malikisi 1)

i. Perekani mikuluwiko iwiri yomwe ili mu nkhaniyi.
_______________________________________________________________________
_______________________________________________________________(malikisi 2)

j. Perekani mutu wa nkhaniyi
_______________________________________________________________(malikisi 1)

## GAWO C (MALIKISI 10)

4. Werengani ka nkhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

**A Gomani:** Odi! Odi! M'nyumbamo

**A Sato** : Eya. Kodi talandira alendo. Chimwemwe, tatenga kachikopa ka mbuzi kaja alendowa akhalepo. Eya, ika pakhondepo. Khalani apa alendo. Nanga muli bwanji wawa, tikuopeni?

**A Gomani:** Ine ndili bwino, ndipo musandiope ndithu. Kunyumbaku tatumiza anyamata ku ndagala. Moti sabata zinayi zikubwerazi simba likhala likuotchedwa.

**Mafunso**

(i) Ndi mtundu wanji wa malonjewa?
_______________________________________________________________(malikisi 1)

(ii) Kodi malonjewa akuchitikira kuti?
_______________________________________________________________(malikisi 1)

(iii) Perekani tanthauzo la mawu oti ndagala.
_______________________________________________________________(malikisi 1)

(iv) Kodi tingathane bwanji ndi kusintha kwa nyengo? Perekani njira imodzi.
_______________________________________________________________(malikisi 1)

(v) Kodi nyali yofiira pamsewu imatanthauzanji?
_______________________________________________________________(malikisi 1)

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:
   a. Chisankho ______________________________________________________________________ (malikisi 1)
   b. Nkhomaliro______________________________________________________________________ (malikisi 1)
   c. Wa ______________________________________________________________________ (malikisi 1)
   d. Kanga ndi wamba ______________________________________________________________________ (malikisi 1)
   e. Wapezwa ______________________________________________________________________ (malikisi 1)

## GAWO D (40 MALIKISI)

**Mafunso 6-10: Sankani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

6.Dziko likolola chimanga chochepa
- **A.** Muonjezi
- C. Mvekero
- B. Mfotokozi
- D. Mlumikizi

7.Mtengo wa mangowu ndi waukulu kwambiri
- A. Mneni
- C. Mfotokozi
- B. Muonjezi
- D. Mfuwu

8.Ku Chawe ndikongola
- A. Muonjezi
- B. Mneni
- C. Mfotokozi
- D. Dzina

9.Ngakhale mwandimenya ndidzibwerabe kwanu.
- A. Mlowammalo
- B. Mfotokozi
- C. Mlumikizi
- D. Dzina

10.Chisomo ndi munthu wabwino.
- A. Mneni
- B. Mlowammalo
- C. Dzina
- D. Mperekezi

**Mafunso 11-15 sankhani magulu amayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

**11.**Phazi lake ndi lalikulu.
- A. Chi-Zi-
- B. Mu-A-
- C. Li-Ma-
- D. Ka-Ti-

12.Namwino uyu ndi wabwino.
- A. Li-Ma-
- B. Ka-Ti-
- C. Chi-Zi-
- D. Mu-A-

13.Utsi ukuchokera kutali.
- A. Mu-A-
- B. I-Zi-
- C. U-Ma-
- D. Mu-Mi-

14.Mulandu uja umangidwa nawo.
- A. Li-Ma-
- B. Mu-A-
- C. Mu-Mi-
- D. U-Mi-

15.Tidaona mvuwu mu mtsinje wa shire.
- **A.** I-Zi-
- **A.** Mu-A-
- **B.** Mu-Mi-
- **C.** Li-Ma-

**Mafunso 16-20 sankhani mitundu ya alowammalo omwe atsekedwa mzere kunsi kwake**

**16.**Malo awa ndi anga
- A. Waumwini
- B. z
- C. Wowerenga
- D. Wamaonekedwe

17.Kodi mwabwera angati
A. Waumwini
B. Wowerenga
C. Woloza
D. Wofunsa

18.zinayi zatsala kwathu.
A. Opatula
B. Oloza
C. Wamgwirizano
D. wowerenga

19.Awo abwera dzulo
A. Waumwini
B. Woloza
C. Wamgwirizano
D. Wakaloza mwini

20.zambiri zidali za ambiya.
A. Woloza
B. Wakaloza mwini
C. Wowerenga
D. Wopatula

**Mafunso 21-25 sankhani mawu ofanana mmatanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwake**

**21**.zifuyo za **a**Bengo zabedwa.
A. Mbewu
B. Ziweto
C. Zovala
D. Nyemba

22.Chidzete chimaonera mayeso
A. Chimunthu
B. Chanzeru
C. Chitsiru
D. Chimphona

23.Iye adachotsa chipala chonse pamoto.
A. Nkhuni
B. Nthalo
C. Mpoto
D. Phulusa

24.Butawo lokongola lija lasweka.
A. Batani
B. Tsamba
C. Duwa
D. Dzino

25.Apita kokatola nkhuni ku gomo
A. Mtsinje
B. Nkhalango
C. Phiri
D. Munda

**Mafunso 26-30 sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi**

**26.**kupalamula vumbwe mkulinga uli ndi nkhuku
**A.** Munthu udzipalamula ukakhala ndi nkhuku
**B.** Munthu usamapalamule ulibe populumukira
C. Kupalamula ulibe nkhuku umapeza mavuto
D. Vumbwe amafuna nkhuku

27.Tsoka msinde chimanga chilinda mwini.
A. Kuchita mwayi
B. Kuchita matama
C. Kuchita tsoka lalikulu
D. Chimanga chimakoma kuposa msinde

28.Mbuto ya kalulu imakula n'tadzaonani
A. Anthu ena amakulitsa nkhani mowonjezera chabe kapena ponena zabodza
B. Anthu amanena zoona zokhazokha kapena zabodza lokhalokha
C. Anthu ena akometsa nkhani yanzawo basi
D. Kalulu amakulitsa nkhani

29.Nyumba ya mwini saotchera mbewa
A. Kwa eni kumakoma kunena miseche
B. Kwa eni mbewa sizikoma
C. Osamadalira zinthu za ena
D. Zanzako zimakoma kudya

30.Linda madzi apite ndiye udziti ndadala
A. Kumachita change pochita zinthu
B. Osamamanyadira ukachitiridwa chabwino
C. Nzako akakuthandiza kumayamika
D. Sibwino kudzitama vuto lisanafike posonyeza kuti latha

**Mafunso 31-35 sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zomwe zili mmusizi**

31.Ndipitabe ku dambweko ngakhale mundiletse.
A. Ya dzina
B. Ya mfotokozi
C. Ya muonjezi

D. Yoyima payokha

32.ndizomveka zomwe mukunenazo

A. Nthambi yoyima payokha
B. Ya mfotokozi
C. Ya dzina
D. Ya muonjezi

33.Achimwene adatola nkhwangwa imene idasosa ija

A. Ya dzina
B. Ya mfotokozi
C. Ya muonjezi
D. Yoyima payokha

34.sindikufuna kuti mundithandize

A. Yamuonjezi
B. Ya mfotokozi
C. Ya dzina
D. Yoyipa payokha

35.sindilowa pokhapokha mutasesemo

A. Yadzina
B. Ya mfotokozi
C. Yamuonjezi
D. Yoyima payokha

**Mafunso 36-40 sankhani mitundu misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

**36.**Tonse tamenyedwa dzulo

A. Wochititsa
B. Wochitidwa poyera
C. Wochitirana
D. Wochidwa m'chibisira

37.Njoka zikuluzikulu zidalumana

A. Wochitsa
B. Wochitirana
C. Wochitidwa
D. Wochititsitsa

38.Iye amasakasaka mkazi wa banja

A. Wochitirana
B. Wochititsitsa

Wobwerezabwereza

C. Wotsutsa

39.mbava ija yapezwa lero

A. Wonyazitsa
B. Wochitidwa
C. Wonchitira
D. Wochitirana

40.Kondwani adakanitsitsa kuti ndiwakuba

**Mafunso 41-45 sankhani chiganizo chomwe chili ndi ziziundikiro za m'kalembedwe zoyenera**
**M'ziganizo zotsatirazi.**

41.

A. Amayi adati,"choka iwe mwana,wakuba"
B. Amayi adati,"choka iwe mwana wakuba!"
C. Amayi adati,"choka iwe mwana wakuba."
D. "Amayi adati" choka iwe mwana wakuba.

42.

A. Chikondi amayenda,monyada.
B. Chikondi: amayenda, monyada.
C. Chikondi amayenda monyada.
D. Chikondi;amayenda monyada.

43.

A. Kodi Nabetha wanyamula miyala ingati?
B. Kodi Nabetha wanyamula miyala ingati!
C. Kodi Nabetha wanyamula miyala ingati
D. Kodi Nabetha wanyamula miyala ingatiu.

44.

A. Popita mutenge Makope, pensulo, ndi lula.
B. Popita mutenge Makope,pnsulo ndi lula
C. Popita mutenge makope, pensulo ndi lula.
D. Popita mutenge mkope pensulo ndi lula.

45.

A. Maliya amakonda kuvina.
B. maliya, amakonda kuvina
C. maliya amakonda kuvina.
D. Maliya amakonda kuvina.

**MAFUNSO ATHERA PANO**